

# Tsiku la Dawat-e-Islami

(Chichewa)



Dawat-e-Islami **DAY 2<sup>nd</sup> September**



# Tsiku la Dawat-e-Islami

Mu Surah Ale Imran, ndime 104, Allah Wamphamvu zonse akuti:

وَلَتَكُنَّ مِنْكُمْ أُمَّةٌ يَدْعُونَ إِلَى الْخَيْرِ وَيَأْمُرُونَ بِالْمَعْرُوفِ وَيَنْهَوْنَ عَنِ الْمُنْكَرِ وَأُولَئِكَ هُمُ الْمُفْلِحُونَ ﴿١٠٤﴾

*Kumasulira kuchokera ku Kanz al- Iman: "Ndipo payenera kukhala gulu la otere mwa inu amene akuitanira (anthu) ku chilungamo, ndi kulamula zabwino, ndi kuletsa zoipa; Ndipo anthu awa ndi omwe ali opambana."*

## Kukhazikitsidwa ndi Kukula

Pogwira ntchito kutsatira ndime yomwe ili pamwambayi, mu September 1981, wotsogolera za uzimu wotchuka komanso katswiri wamaphunziro Achisilamu padziko lonse lapansi, Shaykh Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دامت برکاتُهُمُ الْعَالِيَة, adayambitsa gulu lachipembedzo lotchedwa Dawat-e-Islami lomwe ndi gulu la abwenzi odzipereka. Ndi kutsimikiza mtima kosasunthika, Dawat-e-Islami idakula, kuthana ndi chipwirikiti cha ndale, zionetsero, ndi mikangano. Motsogozedwa ndi madalitso ndi chisomo cha Allah Wamphamvuzonse, Dawat-e-Islami idawala ngati chipilala chowala. Osangokhala ku Pakistan kokha, m'kanthawi kochepe, mzimu wa utumwi wopatulikawu unadutsa malire ndikufalikira padziko lonse lapansi. Pokwaniritsa cholinga chake chabwino, Dawat-e-Islami yakhazikitsa nthambi zazing'ono zoposa mazana atatu, khumi ndi zitatu (313) pansu pa ma dipatimenti okwana makumi asanu ndi atatu (80).

## Utsogoleri ndi Khonsolo Ya Likulu La Bungwe

Motsogozedwa ndi Ameer-e-Ahl-e-Sunnat دامت برکاتُهُمُ الْعَالِيَة Khonsolo Ya Likulu La Bungwe la Dawat-e-Islami imayesetsa kukweza dongosololi. Mosamalira, mwachikondi komanso mwachitsogozo, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat دامت برکاتُهُمُ الْعَالِيَة akuwonetsa chikondi pa

khonsoloyi, kusamalitsa kukula kwake ndikulimbikitsa kupititsa patsogolo machitidwe onse a Dawat-e-Islami.

## **Ntchito Zachipembedzo ndi Maphunziro**

Dawat-e-Islami idakhazikitsa mosamalitsa zikwizikwi za ma Masaajid ndipo ikupitiriza kuthandizira malo opatulika auzimuwa modzipereka. Sikungoyima pokhapa, yafalitsanso kuzindikiritsa kudzera m'masukulu amaphunziro. Madrasa-tul-Madinah ndi Jamia-tul-Madinah ndi njira ziwiri zophunzitsira, pomwe maziko a Qur'an Yopatulika ndi nzeru zachipembedzo zimachulukuka (zimakula).

Ndi masomphenya apamwamba, bungwe ladzipatulira kupanga zikwi za owerenga ndi Osunga pamtima Qur'an yolemekezeka, ma Imam, alaliki, akatswiri ozama ndi maphunziro, ndi ma Mufti, kumanga mizati ya khalidwe ndi kusintha kwa anthu.

Gululi lili ndi anthu ambiri odzipereka, okhala ndi amuna ndi akazi opitirira 500,000 auzimu omwe amachita zinthu zosiyanasiyana. Pafupifupi 46,000 ogwira ntchito odzipereka amakolola zipatso za ntchito yawo, ndipo monga gulu la nyenyezi, miyandamiyanda ya ochirikiza amayang'ana pa cholinga choyambirira chodzikonkanso okha ndi anthu onse padziko lapansi.

## **Dar-ul-Ifta Ahl-e-Sunnat**

Kumbali ya uphungu wachipembedzo, Dawat-e-Islami yakhazikitsa nthambi za 'Dar-ul-Ifta Ahl-e-Sunnat' m'ngodya zngapo za dziko lapansi. M'malo opatulikawa, akatswiri amaphunziro apamwamba, odzadzidwa ndi kakulidwe ka Dawat-e-Islami, amayankha mwachifundo mafunso malinga ndi malamulo Achisilamu, kupereka malamulo Achisilamu ndi zigamulo zamalamulo kudzera m'njira zingapo, monga foni yam'manja, 'email' ndi zina zambiri.

## **Malo Wofufuzafufuza za Chisilamu ndi Dipatimenti Yosindikiza**

Ndi masomphenya wofalitsa maphunziro opatulika, 'Al Madina-tul-Ilmiyyah' (Malo Wofufuzafufuza za Chisilamu), ali ngati kasupe wochulukuka, kufufuza, kukonza, ndi kulemba unyinjira wa mabuku ndi mapepala. Pofufuza mwakuya kwa kumasulira, Hadith, Malamulo Achisilamu, mbiri ya Mtumiki, ndi zolemba zina zolimbikitsa, zolemba zina zopatsa chidwi zimenezi zimakhala ndi uthenga wowunikira.

Mchisomo cha mgwirizano, malowa ali olumikizana ndi ma dipatimenti angapo ang'onoang'ono, odziwika bwino kwambiri mwa iwo ndi dipatimenti ya ulemu ya mabuku a Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ kufananitsa ndi kuwonetsera zida zamtengo wapatali modzipereka kotheratu. Zosindikizidwa zimafalitsidwa kudzera m'dipatimenti yofalitsa mabuku ya Dawat-e-Islami, ya Maktaba-tul-Madinah

## Dipatimenti Yotanthauzira

Mwa chisomo cha Allah Wamphamvuzonse, Dawat-e-Islami ikumasulira mwakhama mabuku achipembedzo m'zinenero makumi anayi ndi mphambu zisanu ndi imodzi (46) padziko lonse lapansi. pakadali pano, dipatimentiyi yamaliza ntchito zopitirira zikwi zisanu ndi ziwiri (7,000) zonse ndipo zambiri mwa izo zidayikidwa patsamba lovomerezeka la webusayiti la Dawat-e-Islami, ndi cholinga chowawongolera Asilamu. Pansi pa dipatimenti iyi, kumasulira kwa Qur'an yopatulika, yotchedwa 'Kanzul Irfan' yokhala ndi zolemba zofotokozerwa 'Ifham-ul-Quran,' kukuchitika m'zinenero makumi atatu (30).

Ndi chisomo cha Allah, kutanthauzira Kanzul Irfan ndi kufotokozerwa kwake 'Ifham-ul-Quran' komanso 'Kanz al-Iman' mziyankhulo za Chingerezi ndi Sindhi zasindikizidwa ndi dipatimenti ya Dawat-e-Islami, Maktaba-tul-Madina.

## Kufikira (anthu) pa Intaneti ndi Maphunziro

Dawat-e-Islami imafikira anthu ndi uthenga wake wolungama kudzera m'kupezeka kwake pa intaneti, [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net), kupereka zothandizira m'zilankhulo zosiyanasiyana. 'Faizan Online Academy' imapereka maphunziro a pa intaneti monga ndondomeko ya maphunziro a Madani komanso kuwerenga ndi kuloweza Qur'an Yopatulika. Maphunziro oposa makumi atatu (30) amatsegula zitseko za kuunikira ngati ngale zanzeru zofikira nyumba za iwo amene akufuna kulandira maphunziro opatulika.

## Kachitidwe ka Maphunziro - Dar-ul-Madinah

M'gawo la maphunziro, monga mlozo wa kuwala kwa kuzindikira, kuphunzira kupyolera M'chingerezi, m'ndondomeko ya Chisilamu yotchedwa 'Dar-ul-Madinah' kumafalitsa kuwala kwake, pakulera maganizo a ana aang'ono kuchokera asanayambe sukulu za nkombaphala mpaka kusekondale. Ndi zikhumbokhumbo zapamwamba,

kachitidweka kamayang'ana kukulitsa chikoka chake kufikira kupitiriza kufunikira kwake ku koleji ndi maphunziro aku yunivesite.

## **Gawo la Luso Lofalitsa mawuthenga (IT)**

Ndi mtima wa ukadawulo pa ntchito zaluso, Dawat-e-Islami ikupita patsogolo paulendo wake wopatulika ndipo yakhazikitsa dipatimenti yochititsa chidwi ya luso lofalitsa mawuthenga (IT), kaphatikizidwe kogwirizana ka maphunziro Achisilamu ndi zodabwitsa za dijito (digital).

Kupyolera m'kugwiritsa ntchito kwa masamba a mchezo komanso tsamba lake la webusayiti la mitundu yosiyanasiyana, (bungweli) limafikira mbali zambiri, kukumbatira miyoyo (ya anthu) kulikonse. Dipatimenti ya IT yapangitsa kuti chuma cha maphunziro Achisilamu chifikire mosavuta kwa anthu kudzera pa intaneti komanso luso la makono. Kudzipereka kumeneku pakuphatikiza miyambo ndi luso la ukadaulo kwadzetsa chipambano cha Dawat-e-Islami pa njira zofalitsa nkhani pa dijito komanso gawo la IT.

## **Kupezeka kwa njira zofalitsira nkhani**

Dawat-e-Islami imapereka uthenga woitanira m'kulungama kudzera mu 'Madani Channel,' kuwulutsa ziphunzitso za Chisilamu mu Urdu, Chingerezi, ndi Bengali pa ma satelayiti akuluakulu asanu ndi awiri. Pogwiritsa ntchito masamba a mchezo a pa Intaneti, Dawat-e-Islami imafalitsa maphunziro Achisilamu, kukhudza miyoyo ya ogwiritsa ntchito intaneti pafupifupi mamiliyoni 450 pofuna kukonzanso (miyoyo yawo). ,

## **Ntchito za Chifundo ndi Zothandiza anthu**

M'gawo la ntchito zothandiza anthu, FGRF (Faizan Global Relief Foundation) yawoneka ngati nyenyezi yowala, pofikitsa ntchito zake za chifundo mnyengo za ngozi zogwa mwadzidzidzi ndi zowawa za anthu mmadera. Pakulimba mtima ndi kudzipereka, FGRF yakhudza miyoyo ya maanja opitirira mamiliyoni 2.6, popereka chakudya ndi chiyeembekezo kudzera m'ndalama, chakudya, ndi zina.

Kukoma mtima kwa FGRF kulibe malire pa maumboni akutengedwa kwa matumba 53,000 a magari othandizira miyoyo ya odwala matenda a kuchepa kwa magari.

## Ma Purojekiti Ena

Chinsalu cha chifundo cha Dawat-e-Islami chikukulirakulirabe. Pakuphatikizidwa ‘Pologalamu ya Dziko Lobiriwira’, (Green World Program) pansi pa pologalamuyi, mitengo mamiliyoni ambiri yabzalidwa. Chinthu chinanso chamtengo wapatali kuchokera ku mbiri yake yabwino ndi 'FRC' (Faizan Rehabilitation Centre), yomwe imatambasula dzanja lake lachifundo kwa ana amasiye ndi ana osowa, kuwalera mosamala.

Ndi zokhumba zapamwamba, (za bungwe) Dawat-e-Islami limalingalira za ‘Nyumba za Madani’ za anyamata ndi atsikana, kulimbikitsa malo opatulika a chikondi ndi kuphunzira. Kuwapatsa mphamvu za luso abambo ndi amayi, kumayala maziko a mabungwe omwe amapanga moyo kukhala m’maloto, kutsekula njira ya tsogolo lowala.

Allah Wamphamvuzonse apereke chipambano ndi kupita chitsogolo kwa Dawat-e-Islami. Amen!

